# PHUNZIRO LA 66

1. Kodi chifukwa chiyani Atsogoleri a Ayuda sanafune kumugwira Yesu pa tsiku la Pasaka?
-Chifukwa chakuti iwo ankadziŵa kuti akamugwira Yesu pa tsiku la Pasaka, anthu aŵawukira iwo.

2. Kodi Yudasi ankadziŵa kuti iye anabadwira mu tchimo, ndipo akufunika Yesu kwa iye ngati Mpulumutsi wache?
-Ayi.

3. Kodi amene anamutsogolera Yudasi kuti amupereke Yesu anali ndani?
-Satana.

4. Kodi chifukwa chiyani Satana anafuna kuti Yudasi amupereke Yesu?
-Chifukwa chakuti Satana amamuda Yesu.

5. Kodi chifukwa chiyani Satana amamuda Yesu?
-Chifukwa chakuti Yesu ndi Mulungu.
-Chifukwa chakuti Yesu amalankhula zowona zenizeni.

6. Kodi chifukwa chiyani Satana anafuna kuti atsogo-leri a Ayuda amuphe Yesu?
-Satana anafuna kuti atsogoleri a Ayuda amuphe Yesu kuti Iye asaŵapulumutse anthu.
-Satana anafuna kuti atsogoleri a Ayuda amuphe Yesu kuti Iye asawononge mphamvu ya tchimo ndi imfa.

7. Kodi aneneri analankhula kuti adzamupereke Yesu ndani?

-Mzake.

8. Kodi nanga Yesu anaperekedwa pa ndalama zingati?
-Makumi atatu a siliva.

9. Kodi Yesu anadziŵa bwanji kuti Yudasi amupereka Iye?
-Chifukwa chakuti Yesu ndi Mulungu, Iye amadziŵa zinthu zonse.
-Palibe chimene Yesu sachidziŵa.

10. Kodi mkate unali bwanji chizindikiro cha thupi la Yesu?
-Thupi la Yesu lidzanyemedwa ndi anthu oyipa ngati m'mene Iye ananyemelanyemela mkatewo.

11. Kodi nanga mpesa ukhala bwanji chizindikiro cha magazi a Yesu?
-Magazi a Yesu adzaturutsidwa ngati m'mene unkaturutsidwira mpesawo kuchokera mu chikho kuti umwedwe.

12. Kodi Yesu analankhula kuti mwazi wache ukhetsedwera yani?
-Yesu analankhula kuti mwazi wache akhetsedwa chifukwa cha anthu ambiri.

-Yesu pamodzi ndi ophunzira ache ataturuka mu mzinda wa Yerusalemu, anapita ku phiri la Azitona ku munda otchedwa Getsemane.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 14:32-36



-Mkulu wa amsembe uja analankhula kuti Iye wanyoza Mulungu.

-Kodi Yesu ananyoza Mulungu?
-Ayi.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 14:65

65-Ndipo ena anayamba kumuthira malovu; kumuphimba nkhope yache, ndikumubwanyula, ndikumati, "Lota!" Kenako omulondera anamutenga ndikumumenya Iye.

-Ngati m'mene Mulungu analankhulila kudzera mwa aneneri mu zaka zambiri zapitazo, Mpulumutsi anayeneradi kumenyedwa ndi kulavulilidwa.

-Mkulu wa amsembe pamodzi ndi akuluakulu a Ayuda anamulamula Yesu kuti aphedwe.

ngati Mulungu Mpulumutsi kudzaŵapulumutsa anthu.

-Pamene Yesu adzabwelenso pa dziko la pansi, munthu aliyense adzamuwona Iye atakhala ku dzanja la manja la Mulungu Atate.

-Pamene Yesu adzabwelenso pa dziko la pansi, munthu aliyense adzamuwona Iye kuti ndi Mulungu.

-Kodi mkulu wa amsembe uja anachita chiyani atamva mawu a Yesu?

Tiyeni tiŵerenge Maliko 14:63-64

63-Ndipo mkulu wa amsembeyo anang'amba zovala zache. Kenako anafunsa kuti, "Kodi tifunilanji mboni zina?"

64-Mwamva mwano wache. Kodi mukuganiza chiyani?"Ndipo onse anamutsutsa Iye namulamula kuti ayenera kufa.

-Kodi chifukwa chiyani mkulu wa amsembe uja anang'amba zovala zache?

-Ayuda akakwiya kwambiri kapena kukhumudwa, unali mwambo wawo ong'amba zovala.

-Kodi chifukwa chiyani mkulu wa amsembe uja anakwiya kwambiri?

-Chifukwa chakuti Yesu analankhula kuti Iye ndi Mulungu.

-Kodi chifukwa chiyani mkulu wa amsembe uja analankhula kuti Yesu ayenera kuphedwa?



32-Ndipo iwo anapita ku malo otchedwa Getsemane, kenako Yesu analankhula kwa ophunzira ache kuti, "Bakhalani pano Ine ndikupemphera.'

33-Ndipo anatenga Peturo, Yakobo ndi Yohane, kenako Iye anayamba kukhumudwa ndikuvutika mu mtima ndithu.

34-Ndipo ananena kwa iwo kuti, "Moyo wanga uli wachisoni kwambiri, kufikira pa imfa. Bakhalani pano, ndipo mudikire."

35-Ndipo Iye anapita mtsogolo pang'ono, nagwa pansi, napemphera kuti ngati kuli kotheka, nthaŵi imeneyo imupitilire.

36-Ndiponso anati, "Abba, Atate, zinthu zonse ndi zotheka ndi Inu. Mundichotsere chikho ichi. Komatu sichimene ndifuna Ine, koma chimene mufuna Inu."

-M'munda wa Getsemane, Yesu anayamba kupenphera, Iye atakhumudwa ndikuvutika mu mtima kwambiri.

-Kodi chifukwa chiyani Yesu anakhumudwa ndikuvutika mu mtima?

-Chifukwa chakuti Iye anadziŵa kuti avutika kwambiri.

-Chifukwa chakuti Iye anadziŵa kuti kuvutika kumene kunkadza kwa Iye, kunali kuvutika kowopsya kwambiri kumene wina aliyense sanakuwoneko.

-Ngakhale kuti Yesu anali Mulungu weniweni, analinso munthu weniweni.

-Kunali kovuta kwambiri kwa Yesu kuti apezane ndi zovuta zowopsya kwambiri zimene zinali kutsogolo

kwache.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 14:37-42

37-Kenako [Yesu] anabwelera kumene kunali ophunzira ache, naŵapeza iwo ali mtulo. Ndipo Iye anati kwa Petulo, “Simoni, ukugona kodi? Kodi unalibe mphamvu yodikira kwa ora limodzi lokha?

38-Dikirani ndipo mupemphere kuti musagwe m’mayesero. Mzimutu ukufuna, koma thupi liri lolefuka.”

39-Ndipo Iye anachokanso, napemphera, nanenanso mawu omwewo.

40-Ndipo Iye atabweleranso, anaŵapenzanso [ophunzira achewo] ali mtulo, chifukwa chakuti maso awo anali olemedwa. Ndipo iwo sankadziŵa chomuyankha Iye.

41-Ndipo Iye anadzanso kachitatu, nati kwa iwo, “Kodi mukugonabe ndikupumula? Kwakwana! Nthaŵi yafika. Onani, Mwana wa Munthu aperekedwa m’manja mwa anthu ochimwa.

42-Ukani! Tiyeni tidzipita! Onani munthu ondiperekayo wayandikira!”

-Yesu atatha kupemphera m’munda wa Getsemane, khamu la anthu linadza ndi malupanga ndi zibonga.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 14:43-46

43-Ndipo nthaŵi yomweyo Iye akulankhula, Yudasi, m’modzi wa khumi ndi aŵiri, anatulukira ndi khamu la anthu, ali ndi malupanga ndi zibonga, atatumizidwa ndi akuluakulu amsembe ndi aphunzitsi a



-Kenako mkulu wa amsembe uja anayima ndikulankhula kwa Yesu.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 14:60-62

60-Ndipo mkulu wa amsembe anayimilira pakati namufunsa Yesu kuti, “Kodi siwuyankha kanthu? Kodi ndi chiyani chimene anthu awa akukuchitira iwe umboni?

61-Koma Yesu anakhala chete, osayankha kanthu. Mkulu wa amsembeyo anamufunsanso Iye kuti, “ Kodi iwe ndi Kilisitu, Mwana wache wa Odalitsika?”

62-Yesu anayankha kuti, “Ndine amene. Ndipo mudzamuwona Mwana wa Munthu atakhala ku dzanja la manja la Wanphamvu zonse, akudza ndi mitambo ya kumwamba. “

-Pamene anthu ankaperekera mawumboni onama a Yesu, Yesu anangokhala chete, osayankha kanthu.

-Kodi chifukwa chiyani Yesu sanayankhe kanthu?
-Yesu anadziŵa kuti Mulungu Atate amutsogolera Iye.

-Yesu anadziŵa kuti Mulungu Atate ndi amene ankayendetsa zonse zimene zinakamuchitikira Iye.

-Kenako, mkulu wa amsembe uja atayankhula kwa Yesu ndikumufunsa Iye kuti ngati ali Kilisitu, Mwana wa Mulungu, kodi Yesu anayankha chiyani?

-Yesu anayankha kuti, “Ndine amene.”

-Pamene Yesu anabwera pa dziko la pansi, anabwera

a milandu onse anafunafuna umboni otsutsana naye Yesu kuti amuphe, koma sanawupeze.

-Kodi chifukwa chiyani atsogoleri a Ayuda sanamupeze Yesu ndi china chilichonse chochimwa?
-Chifukwa chakuti Yesu sanachite china chilichonse chochimwa.
-Chifukwa chakuti Yesu sanachite tchimo lina lililonse.

-Anthu ena anapereka mawumboni otsutsana ndi Yesu, koma nawonso mawumboniwo anali onama.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 14:56-59

56-Ambiri anamuchitira umboni onama, koma umboni wawo siwumalingana.
57-Ndipo ena anayimilira ndikumuchitira umboni onama, nanena kuti:
58-"Tinamumva Iye akunena kuti, Ine ndidzawononga kachisi uyu opangidwa ndi munthu ndipo ndidzamanga wina pa masiku atatu osapangidwa ndi munthu."
59-Koma umboni wawo siwumalinganabe.

-Ngakhale kuti anthu ambiri anapereka mawumboni onama a Yesu, akuluakulu a Ayuda sanapezebe china chilichonse cholakwa ndi Yesu.

-Ngati m'mene Mulungu analankhulira kudzera mwa aneneri mu zaka zambiri zapitazo, mboni zambiri zinaperekadi mawumboni onama okamba za Mpulumutsi.



malamulo, ndi akuluakulu ena.
44-Ndipo omupereka Iye anaŵapatsa chizindikiro ichi: Iye amene ndakampsompsoneyo, ndiye munthu wache; mukamgwire ndipo mukanke naye ali olondedwa."
45-Ndipo atafika kwa Yesu, Yudasi anati, Rabi; nampsompsona Iye.
46-Ndipo anamugwira ndikumumanga Iye.

-Kodi amene ankalitsogolera khamu la anthu amene ananyamula malupanga ndi zibonga anali ndani?
-Yudasi.

-Kodi chifukwa chiyani Yudasi ndi khamu la anthulo anafika kwa Yesu?
-Kudzamugwira Yesu.

-Kodi amene ankamutsogolera Yudasi kukamugwira Yesu anali ndani?
-Satana.

-Kodi ndi ndani wina amene amatsogoleledwa ndi Satana?
-Anthu onse amene amakana kumvera Mawu a Mulungu, nawonso amatsogoleledwa ndi Satana.
-Anthu onse amene sakhulupilira mwa Yesu ngati Mpulumutsi, nawonso amatsogoleledwa ndi Satana.

-Kodi Yudasi anamupereka bwanji Yesu?
-Pomumpsompsona.

-Pamene Yudasi ankamumpsompsona Yesu, anthu amene anali ndi Yudasiyo anamugwira Yesu.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 14:47-49

47-Koma m'modzi mwa anthu amene anayimilira pafupi ndi pamenepo, anasolola lupanga lache, nakantha kapolo wa wamkulu wa amsembe, namudula khutu lache.

48-Ndipo Yesu anati kwa iwo, "Kodi Ine ndi wachifwamba, pobwera ndi malupanga ndi zibonga podzandigwira Ine?

49-Masiku onse ndinali ndi inu m'kachisi ndikukuphunzitsani, ndipo simunandigwire Ine. Koma izi zachitika kuti malemba akwanilitsidwe."

-Kodi Yesu ankatanthawuza chiyani pamene Iye analankhula kuti malemba akwanilitsidwe?

-Yesu ankatanthawuza kuti zonse zimene Mulungu analankhula kudzera mwa aneneri mu zaka zambiri zapitazo, zokamba Mpulumutsi, ziyenera kuchitika.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 14:50

50-Kenako [ophunzira ache onse] anamusiya Iye, nathaŵa.

-Kodi chifukwa chiyani ophunzira a Yesu onse anathaŵa?
-Ophunzira a Yesu ankawopa kwambiri ndiponso sankamvetsetse chifukwa chimene Yesu amagwidwira.

-Kodi ophunzira a Yesu sankamvetsetsa chiyani?



-Ophunzira a Yesu sankamvetsetsa za m'mene Yesu angakhalile Mpulumutsi ngati Iye atagwidwa ndi kuphedwa.

-Ophunzira a Yesu sankamvetsetsa za m'mene Yesu angaŵapulumutsile iwo ngati Iye ataphedwa.

-Kodi anthu amene anamugwira Yesu anamutengera kuti?

Tiyeni tiŵerenge Maliko 14:53-54

53-Ndipo Yesu anamutengera kwa mkulu wa amsembe, ndipo anasonkhananso akulu akulu amsembe, aphunzitsi a malamulo ndi akulu akulu ena.

54-Ndipo Peturo ankamutsatira Iye chapataliko, kufikira atalowa m'bwalo la mkulu wa amsembe. Kumeneko anakhala pansi ndi olondela ndikumawotha moto.

-Anthu amene anamugwira Yesu aja anamutengera Iye kwa wamkulu wa amsembe.

-Peturo ankatsatira potalikirako, koma nayenso ankawopa kuti mwina angagwidwe ndikuphedwa.

-Anthu atapita ndi Yesu kwa mkulu wa amsembe, akuluakulu onse a amsembe pamodzi ndi atsogoleri a Ayuda anakomana kuti amuzenge mulandu Yesu.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 14:-55

55-Ndipo akulu akulu amsembe ndi akulu akulu